M14/1/AXCHW/SP1/NYA/TZ0/XX

22140523

International Baccalaureate®
Baccalauréat International
Bachillerato Internacional

**CHICHEWA A: LITERATURE – STANDARD LEVEL – PAPER 1**
**CHICHEWA A : LITTÉRATURE – NIVEAU MOYEN – ÉPREUVE 1**
**CHICHEWA A: LITERATURA – NIVEL MEDIO – PRUEBA 1**

Friday 9 May 2014 (morning)
Vendredi 9 mai 2014 (matin)
Viernes 9 de mayo de 2014 (mañana)

1 hour 30 minutes / 1 heure 30 minutes / 1 hora 30 minutos

---

INSTRUCTIONS TO CANDIDATES

- Do not open this examination paper until instructed to do so.
- Write a guided literary analysis on one passage only. In your answer you must address both of the guiding questions provided.
- The maximum mark for this examination paper is *[20 marks]*.

INSTRUCTIONS DESTINÉES AUX CANDIDATS

- N’ouvrez pas cette épreuve avant d’y être autorisé(e).
- Rédigez une analyse littéraire dirigée d’un seul des passages. Les deux questions d’orientation fournies doivent être traitées dans votre réponse.
- Le nombre maximum de points pour cette épreuve d’examen est *[20 points]*.

INSTRUCCIONES PARA LOS ALUMNOS

- No abra esta prueba hasta que se lo autoricen.
- Escriba un análisis literario guiado sobre un solo pasaje. Debe abordar las dos preguntas de orientación en su respuesta.
- La puntuación máxima para esta prueba de examen es *[20 puntos]*.


© International Baccalaureate Organization 2014

https://xtremepape.rs/

*Lembani ndemanga pa nkhani* ***imodzi*** *yokha. Poyankha funsoli mugwiritse ntchito mafunso onse awiri amene aperekedwa.*

**1.**

## Amulalatira atsibweni ake

Mawuwa adamudzidzimutsa Katakwe ndi mkazi wake yemwe. Ngakhale mbalame zomwe zinkayimba tinyimbo m'mitengo yapafupi nazonso zinadabwa chifukwa zidakhala chete.

Pampando wa ndakhutagone pomwe adali, Katakwe adakhala tsonga. Naye mkazi wake adadzutsa mutu pamkeka womwe adagona pakhundu pake. Onse pokweza maso adaona kuti mwini mawuwo sadalinso wina koma a Topitopi.

Malume a Katakwewo adatulukira ali mu jekete lothina ndi buluku la fuleya. M'kati adavala malaya ofiyira ndi tayo yayitali yomwe idatulukira palisani ngati lilime la nanzikambe. Poyamba jeketelo lidali loyera, koma panopa, ngati kuti linkatsatira mano a malumewo omwe adali othimbirira n'kachasu, lidali mtundu wakatondo.

M'dzanja lawo lamanzere mudali velemoti yakachasu. Paphunzi lawo lamanja adakolekapo chikwama chomwe mudasuzumira mabotolo atatu.

"Malume, mukufuna pereseyu atiyalutse kapena kutipha?" Katakwe adaphiphiritsa nkhani.

"Phu!" a Topitopi adalavulira pansi. "Pa awirinu, vuto lili ndi ndani? Iweyo kapena mkazi wakoyu?"

"Tsibweni, tamalankhulani motsitsa; pano mpalayini," adapempha Katakwe. "Anthu akamva aziti chiyani?"

"Ndikufuna muchite manyazi kumene!" A Topitopi adayankha kwinaku akupsontha bibida uja.

Katakwe adapuma mozama nakweza manja ake. "Malume, nkhani ngati iyi tisakambirane panja ngati pano; tiyeni m'nyumbamo."

Iwo adawatsatira awiriwo. Atalowa m'nyumbamo, mkazi wa Katakwe adawapempha kuti akhale pampando.

"Sindinabwere kudzacheza," a Topitopi adakana kukhala pansi. "Chomwe ndikufuna kudziwa n'chakuti kodi pakati pa awirinu gocho kapena chumba ndani?"

"Palibe wosabereka," adayankha Katakwe.

"Palibe wosabereka!" Adatsatira monyodola a Topitopi. "Nanga nsalu ya lekaleka ili kuti? Ana ali kuti? Anthu oti mwatha chaka opanda mwana n'kumati ndife obereka? Zadothi!"

Katakwe adaseka kwinaku akugwedeza mutu. "Malume ifeyo panopa tikulera. Tidzabereka tikatolera katundu pakhomo pano."

"Zamkutu!" A Topitopi adatsutsa. "Munthu amalera alibiretu ndi mwana yemwe?"

"Tsibweni, tawonani m'mene mulili m'nyumba muno; mulibe chilichonse. Ifeyo tikufuna tikonzekere bwinobwino tisanakhale ndi…"

"Chete!" Adamudula malume akewo akutulutsa chibotolo n'kuchiyika patebulo. "Awa ndi mankhwala obereketsa. Muzikhutchumula, akachita thovu muzimwa. Katatu patsiku."

"Malume…"

"Ndati chete!" Adazaza a Topitopi akutulutsa chibotolo chachiwiri kuchokera m'chikwama muja.

"Mtera uwu ndi nkhondo kubedi. Mayi, usiku uliwonse musadalowe kuchipinda kukagona, muziwonetsetsa kuti mwamwa."

Sadadikire kuti ayankhidwe, iwo adatulutsanso chibotolo chomaliza, natembenukira kwa katakwe. "Umu ndiye muli mutuwo; mthibulo. Mphwanga macheza asadayambike, uziwonetsetsa kuti wamwa muti umenewu."



https://xtremepape.rs/

"Malume…"

"Osandisokeneza! Ikadutsa miyezi itatu mudzandiwonanso ndikutulukira," a Topitopi adadukiza napanga chizindikiro ngati akucheka pakhosi pawo.

"Ndikadzapeza zinthu zizanasinthe, mudzadziwiretu kuti banja lathera pomwepo. *Finish*, lamara, lasira, limasile, latha!"

Popanda kutsanzika, iwo adatuluka momenyetsa chitseko.

L Kadzitche, *Katakwe zaka* 10 (2011)

(a) Muli ndi maganizo anji pa za mikangano ya pakati pa mibadwo yosiyanasiyana ndipo kodi mkangano wasonyezedwa bwanji munkhaniyi?

(b) Unikani momwe mlembi wagwiritsira ntchito luso losiyanasiyana polemba (monga kukambitsana) ndipo momwe lusoli lathandizira pa tanthauzo la nkhaniyi.



https://xtremepape.rs/

**2.**

**Kuli kwathu**

Kukhosi kwaumaku ndili kwathu
Likanafewetsa ndi thovu lokha
Thovu losefukira, kuyenderera
Chipanda cha mowa choyangatidwa bwino
Uli pachiphaka, pankhokwe yedzekeke
Ndi thovu likanafewetsa
Kachipanda kachindimba kali:
    Phi-phi-thi, phi-phi-thi, phi
    Phi-phi-thi, phi-phi-thi, phi
    Phi-phi-thi, phi-phi-thi, phi
    Phi-phi-thi, phi-phi-thi, phi
Azimayi atatsetseretsera zilundu
Zawo chambali apa, zingoli
Akuvomerezana ndi azibambo
Ena onse natsirira mang'ombe navina
Inde ndi thovu nthuni
Likanafewetsa kummero kwaumaku
Thovu losefukira chipanda
Thovu loziziritsa kukhosi
Thovu losesa fumbi kuti
Ukonkhe bwino moyera, kukhosi
Kumveke libwidi
Ndipo malovu ali mkamwa lengezuwa
Ndi thovu la kaphala, ayi ndithu
Bwenzi mgwidyo numveka bwino
Kuli kwathu nsenga tikanatafunira
Thovu la thikhwithikhwi lili
Thwanithwani; kupenya oyimba ng'oma,
    thi-thi-thi
    thi-thi-thi
'Akabango' ndi mluzu zili pakamwa
Koma kuno, ayi mbale, ngakhale
Nsengwa zotafunira, kaya nthungululu
Yokha ata! zingoli zimene ndi za wena,
Kwina! Likhala thovu limene
Ndi tinthubwithubwi, tophenima
Ndi kamphepo kayepiyepi nanga
Thovu lidzinga la sopo yamakaka

Jack Mapanje, *Akoma Akagonera* (1986)



https://xtremepape.rs/

(a) Kodi mukuganiza kuti woyankhula m’dakatuloyi ali ndi maganizo anji pa za moyo wa kumudzi kwawo kapena wa kwa eni ndipo maganizo amenewa asonyezedwa bwanji m’ndakatuloyi?

(b) Unikani momwe mlembi wagwiritsira ntchito zithunzithunzi m’ndakatuloyi ndipo kuti zikuthandizira bwanji pa tanthauzo la ndakatuloyi yonseyi.



https://xtremepape.rs/